**Zekariya 14 :3,4; "Pamenepo Yehova adzaturuka nadzachita nkhondo ndi amitundu aja, monga anachitira nkhondo tsiku lakudumana. Ndi mapazi ache adzaponda tsiku lomwelo pa phiri la Azitona, liri pandunji pa Yerusalemu kum'mawa, ndi phiri la Azitona lidzang'ambika pakati kuloza kum'mawa ndi kumadzulo, ndipo padzakhala chigwa chachikulu ; ndi gawo lina la phirilo lidzamuka kumpoto, ndi gawo lina kumwela. "** ( Kubweranso kwachiwiri kwa Yesu Mkhristu kudzatsonkhezeredwa ndi kufuna kuonongedwa kwa Yerusalemu ndi amitundu).

Ambuye adzabwera kufuna kuteteza mzinda wa Yerusalemu ndi anthu ache. Adzabwera monga Ambuye Mulungu wa Israeli.

**Zekariya 14 :11; "Ndipo anthu adzakhala m'menemo, ndipo sipadzakhalanso kuonongetsa ; koma Yerusalemu adzakhala mosateketseka. "** ( Yesu adzabweretsa mtendere padziko lapansi).

**Zekariya 14 :12 ; " Ndipo mliri umene Yehova adzakantha nao mitundu yonse ya anthu imene idathira nkhondo pa Yerusalemu ndi uwu : nyama yawo idzaonda akali chiriri pa mapazi awo, ndi maso awo adzapuala m'funkha mwao, ndi lilime lao lidzanyala m'kamwa mwao. "** ( Yesu Mkhristu adzatulutsa mphamvu zake zonse pa anthu oipa ndipo pomwepo adzaonongedwa kotheratu).

**Obadiya 1:15; "Pakuti tsiku la Yehova layandikira amitundu onse ; monga unachita iwe, momwemo adzakuchitira ; chochita iwe chidzakubwerera pamtupako. "**

Kuti mulandire chikondi cha Mulungu ndi chitsimikizo cha moyo wosatha, khulupirirani pamene mukupemphera pemphero monga ili :

*"Ambuye ndikulapa tchimo langa ndikutembenukira kwa Yesu Mkhristu. Ndikhulupirira kuti mchikondi chanu, munatumiza Yesu kuti afe pamtanda ndikukhetsa mwazi wache kupereka dipo la tchimo langa. Ndikhulupiriranso kuti anauka kwa akufa. Ndikubvomereza tsopano kuti Yesu ndi Ambuye ndi mpulumutsi wa moyo wanga. Tsopano popeza Yesu ndi Ambuye wanga, ndili ndi chitsimikizo cha moyo wosatha, ndipo inu Ambuye ndinu tsopano Atate wanga. Zikomo mu dzina la Yesu. "*

*Atate Mulungu wanga, munatumizanso Yesu kuti adzachize osweka mtima. Ndikupemphani kuchiza mtima wosweka wa onse akuwerenga mau awa. Kusweka kwa mtima chifukwa chotaya okondedwa, chifukwa cha ziwawa, chifukwa cha mantha, kukhumudwa, kusowa abale, banja loonongeka, kugwiriridwa ndikusokonezeka. Chonde Ambuye masulani onse amaganizidwe omangidwa ndi malinga a uchimo. Atate, masulani onse ophinjika ndi mdierekezi mziphinjo zosiyanasiyana. Ndipo ndi chikondi chanu chopanda malire, masulani wina aliyense wokhala ndi maganizo ofuna kuzipha, kapena onse omangidwa ndi nchitidwe wogwiritsa ntchito mankhwala osokoneza ubongo. Atate ndikupempha kuti aliyense alaweko chikondi chanu chachikuluchi, chimwemwe chanu komanso mtendere wanu. Amen*

Nkhondo yomenyeredwa pa Yerusalemu siyongopitirira ai. Idzatha monga Baibulo linalembera. Mu chaka cha 33AD, Yesu Mkhristu asanafe pa mtanda, ananena kuti tiyang'anire pa Yerusalemu chifukwa kutha kwa nthawi komanso kubwera kwache kwachiwiri kudzatsimikizika pa nkhondo zomwe zidzamenyedwe pa mzinda wa Yerusalemu. Zomwe tikuona lero pa Yerusalemu ndi umboni weniweni wotsimikidzira kubweranso kwachiwiri kwa Yesu Mkhristu. Zonsezi zikusonkhezera kukwaniritsa maulosi ndi uneneri wa Baibulo.

...... **ndipo mapazi a anthu akunja adzapondereza kufikira kuti nthawi zao za anthu akunja zakwanira.**


Chaplain John P McTernan

USA Prophecy. com

Brochures : MCT911@aol.com


# MKHONDO YOTSILIZA PA YERUSALEMU NDIKUBWERANSO KWACHIWIRI KWA YESU KHRISTU



**Luka 21 :24 ; Ndipo adzagwa ndi lupanga lakuthwa, nadzagwidwa ndende kunka ku mitundu yonse ya anthu ; ndipo mapazi a anthu akunja adzapondereza kufikira kuti nthawi zao za anthu akunja zakwanira. "**



M’zikiti wa  Al-Aqsa

Pa 7 October mchaka cha 2023, gulu lotchedwa Hamasi linathira nkhondo dziko la Israeli ndikupha ndi kuvulaza zikwi za anthu komanso kutenga mazana a anthu ku ukapolo. Gulu la Hamasi linati nkhondoyi akuimenya molunjikitsa mzinda wa Yerusalemu ndipo anatchula nkhondoyi kuti ndiyotetezera mzikiti wotchedwa Al Aqsa. Mzikiti umenewu uli penipeni pamene panali kachisi wa Yehova ku Yerusalemu. Gulu la Hamasi linapempha asilamu onse kuti athandizane pa nkhondo yomenyana ndi Israeli ; nkhondo yotetezera mzikiti wa Al Aqsa komanso Yerusalemu. Ngakhale nkhondoyi inayambira dera lotchedwa Gaza, koma maso awo anali pa Yerusalemu.

Ponena kuti nkhondoyi ikumenyedwa chifukwa cha Yerusalemu, ndizopatsa chidwi kwambiri potengera kuti Baibulo likuululanso maulosi odabwitsa okhuzana ndi mzinda umenewu onena za nkhondo ziwiri zomwe zizamenyedwe kumapeto a nthawi komanso kubweranso kwa Yesu Mkhristu. Zonsezi zochitikira mu mzinda womwewu wa Yerusalemu.

Yerusalemu ndiwosiyana ndi mizinda ina. Ndiwapaderadera. Mkatikati mwa zaka za mma 1000BC, mfumu Davide anaupanga mzinda umenewu kukhala likulu la dziko la Israeli ndipo mwana wache Solomoni, anamanga kachisi wapamwamba kwambiri mu mzinda womwewu. Mchaka cha 586BC, a ku Babulo anaonongeratu mzindawu pamodzi ndi kachisi yemwe. Anthu anatengedwa ukapolo ndipo anabwereranso kwao patatha zaka makumi asanu ndi awiri (70). Kumapeto kwache, mzindawu ndi kachisi yemwe zinamangidwanso.

Ndipo mchaka cha 70AD, mzindawu ndi kachisi yemwe zinaonongedwanso kotheratu, koma nthawi iyi boma la chiroma ndi lomwe lidaononga. Ayuda anapitikitsidwa ndi kumwazikana pa dziko lonse lapansi, ndipo Israeli linasiya kukhala dziko ndinso Yerusalemu kukhala likulu lache. Pa 14 May, mchaka cha 1948, Israeli linakhalanso dziko lobvomerezeka zomwe analosera kale aneneri. Mneneri Zekariya polemba mchaka cha 520 BC

analengeza kuti kutsogolo kwa nthawi, Yerusalemu adzapangidwanso kukhala likulu la dziko la Israeli ndipo nkhondo zazikulu za dziko lonse zizamenyeredwa pa mzindawu. Nkhondo yotsirazayo ndi yomwe idzatsonkhezere kubweranso kwachiwiri kwa Yesu Mkhristu. Mulungu woyera wa Israeli yekha ndi yemwe adzatetezere Yerusalemu.

**Zekariya 12 :9 ; “Ndipo kudzachitika tsiku lomwelo, ndidzayesa kuononga a mitundu onse akudza kuyambana ndi Yerusalemu. “** Monga mneneriyu ananenera, mchaka cha 1967 Yerusalemu anakhalanso likulu la Israeli patatha zaka zokwana 1897chiongedwereni ndi Aroma. Mphamvu zomwe zili ndi Baibulo monga mau a Mulungu zikuonekera kudzera muulosi wokhudzana ndi mzinda umenewu. Kukwaniritsidwa kwa maulosi kukuonekera ndi kuyeseredwa pa Yerusalemu, kumene kukukhazikitsa Baibulo kukhaladi mau a Mulungu. Zomwe zitsatire mumndandanda wa zochitika malingana ndi maulosi, ndi nkhondo yoononga mzinda wa Yerusalemu. Maiko ambiri ali kale molimbana ndi Yerusalemu ndipo maiko ena ambiri akutsatira. Zolosera zonse zakwaniritsidwa tsopano ; kuti Israeli ndi dziko lokhazikika lokhalanso ndi gulu la mphamvu la asirikali. Chiheberi tsopano chakhalanso chilankhulo chao chobvomerezeka, komanso Yerusalemu kukhala likulu lache.

Baibulo likuchenjeza maiko kuti asapute Yerusalemu, koma chifukwa cha kusakhulupirira, adzaputa Yerusalemu ndikuonongedwa okha kotheratu.

**Zekariya 12 :2,3 ; “Taonani ndidzaika Yerusalemu akhale chipanda chodzandiritsa kwa mitundu yonse ya anthu yozungulirapo, ndipo chidzafikira Yuda yemwe pomangira misasa Yerusalemu. Ndipo kudzachitika tsiku ilo, ndidzaika Yerusalemu akhale mwala wolemetsa mitundu yonse ya anthu, onse akuusenza adzadzilasa nao ; ndi amitundu onse apadziko lapansi adzasonkhana kutsutsana nao. “** Chifukwa choti Israeli ali ndi gulu la mphamvu la asirikali, maiko onse odzungulira adzaonongedwa psiti.

**Zekariya 12 :6; “Tsiku ilo ndidzaika akalonga a Yuda ngati phale la moto pansi pa nkhuni, ndi ngati muuni wamoto mwa mitolo ya tirigu ; ndipo adzatha mitundu yonse ya anthu pozungulirapo, ku dzanja la manja ndi lamanzere ; ndipo Yerusalemu adzakhalanso m’malo mwache, m’Yerusalemu.”**

Maiko amene Baibulo likunena kuti adzaonongedwa kotheratu ndi ;  Palestina, Yordano, Lebanoni, Syria ndi Aiguputo komanso Iraq ndi magulu ena ankhondo omwe anagwirizana kumenya nkhondo ndi Yerusalemu

**Nkhondo yotsiraza pa Yerusalemu ndi kubweranso kwachiwiri kwa Yesu Mkhristu** :

**Zekariya 14 :1 ; “Taonani likudza tsiku la Yehova, limene zofunkha zako zidzagawanika pakati pako.”**  ( Tsiku la Ambuye ndi mau a m’baibulo ndipo amatanthauza kubweranso kwachiwiri kwa Yesu Mkhristu).

**Zekariya 14 :2; “Pakuti ndidzasonkhanitsa amitundu onse alimbane ndi Yerusalemu ; ndipo mudziwo udzalandidwa, ndi nyumba zidzafunkhidwa, ndi akazi adzakakamizidwa ; ndi limodzi la magawo awiri la mudzi lidzatuluka kumka ku ndende, koma anthu otsala sadzaonongeka m’mudzimo. “** Yerusalemu akuonongedwa popanda chiyembekezo).